FOR MORE INFO CONTACT;

rdgmissions@charter.net

www.icotb.or

ULAMULIRO PA CHIPEMBEDZO

Pamene Mulungu anaona kuti ana a Israyeli akuyamba kusamvera Iye, Iye analankhura nawo kudzera mwa Mose ndipo anawachenjeza kuti adzaukitsa munthu wonga Mose kuti akalankhule nawo. Amene samvera mau Ake adzaonongeka (Deuteronomo 18:15-19)

Lonjezo limeneli kwa ana a Israyeli linakwaniritsidwa pa kubadwa kwa Ambuye Wathu Yesu Khristu (Machitidwe 3:19-26). Iye anabadwa kuti awombole dziko. Koma anakanidwa ndi ana a Israyeli amene anakulira pakati pawo.

Tsiku Lina mu utumiki Wake wa padziko lapansi Ambuye wathu anatenga atatu a ophunzira ake nakwera m'phiri lalitali ***"Ndipo anasandulika pamaso Pao. Ndipo zobvala zake zinakhala monyezimira zoyera mbu; monga ngati muomba wotsuka nsaru pa dziko lapansi sangathe kuziyeretsai. Ndipo anaonekera kwa iwo Eliya ndi Mose, alikulankhulana ndi Yesu. Ndipo Petro anayankha, nanena ndi Yesu, Rabi, kutikomera ife kukhala pano; ndipo timange misasa itatu; umodzi wa Inu, ndi wina wa Mose ndi wina wa Eliya. Pakuti sanadziwe chimene adzayankha; chifukwa anachita mantha ndithu. Ndipo panadza mtambo wakuwaphimba iwo; ndipo mau mumaturuka m'mtambomo, kuti, Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa; mverani Iye"*** (Marko 9:2-7). Tanthauzo lake nchiyani? Mose anaimira chilamuro. Anthu sayeneranso kutsatira chilamuro cha Mose ngati njira yopembedzera Mulungu. Kusunga sabata, kupereka chakhumi, nsembe za nyama ndi nyimbo zoimbira zida sizifunikiranso. Eliya ankaimira aneneri amene analankhura za kubwera kwa Mpulumutsi pa dziko lapansi kuchokera mu mbewu ya Davide. Tsopano popeza Mpulumutsi wabwera,

anthu sayenera kubwerera ku chilamuro ndi aneneri, koma kumvera mawu a Yesu Khristu!

Zimene Khristu ananena sizili zake,koma mawu ochokera kwa Mulungu Atate. ***"Ndipo ngati wina akumva mawu anga, ndi kuwasunga,Ine sindimweruza; pakuti sindinadza kudzaweruza dziko lapansi, koma kuti ndipulumutse dziko lapansi. Iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mawu anga, ali naye womweruza iye, mau amene ndalankhula, iwowa adzamweruza tsiku lomariza. Pakuti sindinalankhula mwa Ine ndekha; koma Atate wondituma Ine, yemweyu anandipatsa Ine lamulo, limene ndikanene, ndi limene ndikalankhule. Ndipo ndidziwa kuti lamulo lake liri moyo wosatha; chifukwa chake zimene ndilankhula, monga momwe Atate wanena ndi Ine, momwemo ndilankhula"***(Yohane 12:47-50).

Anthu ambiri samvera mawu a Khristu. Ngakhale anthu achipembedzo apatuka pa mawu a Khristu ndi kulowetsa maganizo awo. Iwo saganiza kuti Khristu anali wolondola pamene anati: ***"Ndidzakhazika mpingo Wanga"*** (Mateyu 16:18). ***"Wanga"*** amasonyeza umwini. Nzolakwa kothera kuti munthu kapena gulu la anthu lipange chipembedzo chawochawo ndi kulambira Yehova kumeneko. Yesu anati: ***"M'mera wonse, umene Atate wanga wa kumwamba sanaubzala, udzazulidwa. Kawalekeni iwo, ali atsogoleri akhungu. Ndipo ngati wakhungu amtsogolera wakhungu, onse awiri adzagwa m'mbuna"***(Mateyu 15:13-14). Oyambitsa mipingo ya anthu ali atsogoleri akhungu. Amene akupembedza m'menemo ndi otsatira akhungu. Ichi ndi chifukwa chake Yesu anachenjeza: ***"Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye , Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa kumwamba; koma wakuchitayo chifuniro cha Atate wanga wa kumwamba. Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kuchita m'dzina lanuso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, sindinakudziwani Inu nthawi zonse; chokani kwa Ine, inu akuchita kusayeruzika!"*** (Mateyu 7:21-23).

Pa chiweruzo, Yesu adzakana anthu ena, osati chifukwa chakuti sanamupembedze, koma chifukwa chakuti sadachita monga mwa chifuniro Chake. Mulungu analonjeza kumanga nyumba(Yesaya 2:2-3). Nyumba iyi ndi imene Khristu anaitcha ***"mpingo wanga"***. Yesu anagula mpingo uwu ndi mwazi Wake, ***"Tadzichenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira, kuti muwete mpingo wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa Iye yekha"*** (Machitidwe 20:28). Palibe amene ali ndi ufulu wopanga mpingo wina uliwonse kapena kuutcha dzina liri lonse la kusankha kwake.

Tiyeni tilemekeze ulamuliro wa Mulungu! Tisaonjezere zinthu zimene Mulungu walamula! Tisachotsere zinthu zimene Mulungu walamula! (Chibvumbulutso 22:18,19). Ngati sitilemekeza ulamuliro wa Mulungu wopezeka m'baibulo, sitingapulumuke.

Kodi mwapulumutsidwa? Yesu anati, ***"amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa: koma amene sakhulupirira adzalangidwa"*** (Marko 16:16), Bwanji osakhulupirira ndi kubatizidwa lero?